# Anthu Amene Anayenda Ndi Yesu

milton cunningham

2. Ngati munthu afuna kukhala ndi moyo wosatha ayenera kukhala wofuna kusiya zonse zimene zimuletsa kumvera Kristu. Kukhala wophunzira wa Yesu uyenera kukhala womvera. Siungathe kukhala monga mmene Mulungu afunira kuti iwe ukhale ngati uli ndi mtima wogawika. Yesu akhale woyamba. Ticite zinthu zimene Iye afuna kuti ife ticite.

3. Yesu sangathe kuuza munthu kuti amukhulupilire Iye. Yesu siayesa kutipanga ife kuti tikhulupilire. Anatifera ife ndipo atikonda ife, koma munthu ayenera kukhulupilira asanakhale wakuphunzira wa Yesu Kristu.

MAFUNSO:

1. Cifukwa ciani mnyamata uyu anacoka kwa Yesu?
2. Kodi munthu acite ciani kuti akhale mkristu?
3. Cifukwa ciani munthu wamtima wogawika sangathe kukhala ophunzira wa Yesu?

-ooOoo-



ZA MKATIMU


| Phunziro | | Tsamba |
|---|---|---|
| 1 | YESU NDI BARTIMEYU | 1 |
| 2 | YESU NDI MUNTHU WODWALA MANJENJE | 5 |
| 3 | YESU NDI MKAZI WACIGOLOLO | 10 |
| 4 | YESU NDI MKAZI WODWALA | 14 |
| 5 | YESU NDI ZAKEYU | 18 |
| 6 | YESU NDI WAKHALE | 22 |
| 7 | YESU NDI MKAZI WA KU SAMARIYA | 26 |
| 8 | YESU NDI NIKODEMO | 31 |
| 9 | YESU NDI MUNTHU WOSAONA CIBADWIRE | 35 |
| 10 | YESU NDI MUNTHU KU THAMANDA | 39 |
| 11 | YESU NDI MUNTHU WA KU GADARA | 43 |
| 12 | YESU NDI MBALA PA MTANDA | 47 |
| 13 | YESU NDI MNYAMATA WACUMA | 51 |

ndipo Buku Lopatulika linena kuti "Anamkonda". Mnyamatayu anaoneka kuti anali munthu weni weni m'maso mwa Yesu. Pamenepo Yesu anati pali cinthu cimodzi cimene ulibe. "Cinthu cimodzi cikusowa." Pita tsopano Yesu anatero nugulitse zako zonse. Utagulitsa zonse pita upatse ndaramazo anthu aumphawi. Ngati ucita cimeneci cuma udzakhala naco ca kumwamba. Ndipo pamene wagulitsa zako zonse ndikupatsa aumphawi ubwerenso nusenze mtanda nunditsate Ine.

Awa anali mau obvuta kwambiri kwa mnyamata wacuma uja. Ici sakanacitha kucita. Yesu anadziwiratu cobvuta cace ca mnyamatayu. Yesu anali kuuza mnyamatayo, kuti, ulikulandira ulemu kwa anthu cifukwa ca zinthu zimene siucita. Siupha, siucita cigololo, siuba, siubvuta anthu ena. Pamenepo Yesu anati, ndifuna kuti iwe upite ndipo ukacite cinthu cabwino kwa anthu. Pita nugulitse zinthu zako zonse nuthandize nazo anthu aumphawi. Ngati ufuna kuti ukhale wakuphunzira wanga Yesu anatero kwa iye, ucite zoposa kusunga lamulo kokha ---- udzipereke wekha.

Pamene mnyamata uja anamva ici anali wacisoni kwambiri. Ici cinali cinthu capatali kwa iye. Iye anakonda cuma cace. Sanafuna kuzicotsa zinthu zace. Ndipo anacoka ndi mtima wacisoni

MAPHUNZIRO:

1. Moyo wosatha sungapezeke pakusunga lamulo. Cili cinthu coona kuti iwo amene akonda Yesu ayenera kusunga lamulo, koma sicoona kuti ngati wina asunga lamulo ndiye kuti akonda Yesu. Kukhala wophunzira wa Yesu ndi kukhala ndi moyo wosatha munthu ayenera kulapa macimo ndi kukhulupilira mwa Yesu Kristu.

analibe nao kanthu iwo. Anadziwa kuti akanamuseka. Ici sicinamudetse nkhawa. Kuposa kanthu kena kali konse iye anafuna kulankhula ndi Yesu. Nthawi zambiri anthu amaopa kudza kwa Yesu. Amaopa cifukwa siafuna kuti anthu ena awaseke. Mnyamata uja sadasamala za mau ena ali onse amene anthu ena akananena. Anafuna cinthu cimodzi. Iye anafuna kuona Yesu ndi kulankhula naye. Anaonetsetsa zocita zace za Yesu ndi kumva zolankhula zace, tsopano anafuna kulankhula kwa Iye.

"Mphunzitsi wabwino,ndidzacita ciani kuti ndilandire moyo wosatha?" Mnyamata wacuma uyu analemekeza Yesu kwambiri. Iye anamucha Yesu "Rabi." Anthu ambiri anali kuchula dzina lakuti "Rabi" kwa anthu okalamba okha. Unali ulemu waukuru. Koma mnyamata wacuma uyu alikuitana munthu wamsinkhu wofanana naye kuti Rabi. Anafuna kuti Yesu amuuze mmene akanapezera moyo wosatha. Analindi cuma cambiri koma analibe mtima wosangalala. Anadziwa kuti cinthu cina cinali kusowa m'moyo mwace. Iye anaona kuti anali kusunga malamulo. Sanacimwire wina ali yense. Komatu, mumtima mwace sanali wosangalala. Ici ndico cifukwa cace cimene anadzera kwa Yesu. Anadza kudzafunsa Iye cimene iye akanacita kuti akhale ndi mtendere wa Mulungu mumtima mwace.

Yesu anati kwa mnyamatayo, "Usandiche Ine wabwino." Yesu anali kumuuza mnyamata uja kuti Iye anali woposa "Mphunzitsi wabwino." Iye anali Mulungu. Mnyamata uja anafuna kumuona Iye monga Mwana wa Mulungu wopanda cimo

Pamenepo Yesu anati kwa iye, Udziwa malamulo --- usacite cigololo; usaphe; usabe; usanene bodza; usanene umboni wonama; lemekeza atate ako ndi mai ako." Pamenepo waweruza wacinyamatayo anati zonsezi ndinasunga. Sindinaononge lamulo limodzi lonse la awa. Pamene ali kuyankha Yesu anali kumuyang'anitsitsa



PHUNZIRO 1

## YESU NDI BARTIMEYU

MAU A-MULUNGU: Mateyu 20:29-34; Marko 10: 46-52; Luka 18: 35-43.

MAU A PA MTIMA:

"Ndipo Yesu anati kwa iye, Muka, cikhulupiliro cako capulumutsa iwe."

Marko 10:52.

### COZIZWITSA

Yesu anali pa ulendo. Anali kucokera ku Galileya kupita ku Yerusalemu. Pamene anali pa ulendo wace wopita ku Yerusalemu Iye anadzera m'mudzi wa Yeriko. Yesu anadzeranso njira imeneyu kale. Koma ulendo uwu unali wosiyana ndi woyambawo. Cifukwa ulendo uwu unali wotsiliza kuti Yesu ayende kupyola Yeriko. Yesu anali pa ulendo wace kupita ku Yerusalemu kukafa pa mtanda.

Pamene Yesu anali kuyenda mumseu tsiku limenelo anthu ambiri anamutsata Iye. Ena anamutsata Iye cifukwa anali kumukonda. Ena anamutsata Iye cifukwa anafuna kuona zinthu zimene Iye anali kucita. Ena anamutsata cifukwa iwonso anali kupita ku Yerusalemu.

Pemene Yesu anali kulowa m'mudzi wa Yeriko pa mseu panaimilira munthu wakhungu wopemphapempha. Dzina lace anali Bartimeyu. Tsiku ndi tsiku munthu wina anali kumutsogolera pa malo pena pamene anali kutha kuimapo ndi kupempha. Sanatha kugwira nchito. Anali wakhungu. Masiku ace anatha ali kuima pa mseu kupempha ndarama kwa anthu aulendo amene anali kupita pa njira imeneyi. Anali wakhungu wopemphape-

mpha wopanda thandizo ndipo wopanda ciyembekezo.

Pa tsiku ili, pamene Bartimeyu anali kuimilira pa mbali pa mseu ali kupempha anamva mau a cilendo. Anamva phokoso la kuyenda ndi kulankhula kwa anthu pamene anali kuyenda ndi Yesu kulowa mu Yeriko. Cifukwa sanali kuona, iye sanadziwa kuti kapena zinali zoyenera kuopa kapena kukondwera nazo. Kodi anthu amenewa anali abwenzi ace kapena adani ace? Kodi akadamuthandiza kapena kumupweteka?

Pamene gulu la anthu linafika pafupi ndi malo kumene kunali kuimilira Bartimeyu munthu wakhunguyo anayamba kufunsa, "Kodi kuli kucitika ciani?" M'modzi wa m'khamu la anthulo anadzera pafupi ndi Bartimeyu ndipo mkanjo wa munthuyo unakhudza dzanja la Bartimeyu. Mofulumira Bartimeyu anagwira mkanjowo ndipo anaugwiritsa kwambiri. "Undiuze, mnzanga," iye anatero, "Kuli kucitika cinai?" Mlendoyo anatembenukira kwa munthu wakhunguyo nati, "Kodi sudziwa, Yesu wa ku Nazareti ali kupita m'njiramu."

Iyi inali mbiri yabwino kwa Bartimeyu. Sanamuone Yesu, koma kawiri kawiri anamva za mmene Yesu anacilitsila ndi kuthandiza anthu. Anayamba kuganizira, ndikadangolankhula naye kokha." Ngati Yesu akadandiona kokha akadandithandiza. Ndi ciyembekezo ici mumtima mwa Baritmeyu anayamba kuitana, "Yesu, Mwana wa Davide, mundicitire cifundo ine." Anaitanabe kwa Yesu osalekeza. "Yesu mundicitire cifundo ine." Mokwezabe mau anaitana Yesu pamene Iye anali kupita m'njira.

Ndipo posapita nthawi Yesu anaima. Anthu amene anali kukhala m'Yeriko anayesa kumuletsa kuti akhale cete Bartimeyu. Koma sanawamvere. Ndipo tsopano. Yesu anamva kuitana kwace. Pamenepo Yesu anauza



PHUNZIRO 13

## YESU NDI MNYAMATA WACUMA

MAU A MULUNGU: Mateyu 19:16-22; Marko 10: 17-31; Luka 18: 18-30.

MAU A PA MTIMA:

"Yesu anamuyang'ana iye, namkonda, ndipo anati kwa iye, cinthu cimodzi ucisowa."
Marko 10: 21.

### MBIRI YACE

Mnyamata wowenuza, wacuma, anali munthu wodziwika kwambiri. Pa nthawi imene anakomana ndi Yesu anali ndi zaka makumi atatu. Yesu analinso wa zaka makumi atatu. Anali pafupifupi a msinkhu umodzi koma anali wosiyana kwambiri.

Oweruza wacinyamata uyu anali wacuma cambiri ndipo Yesu anali wopanda cuma. Sicinali capafupi kwa oweruza uyu kubwera kwa Yesu. Anali wamalo apamwamba kwambiri pakati pa anthu anzace. Anali wamkuru wa m'Sunagoge. Anali wacuma cambiri. M'masiku amenewo anthu oweruza ndi anthu acuma sanamkonda Yesu. Komatu, mnyamata uyu, anafuna kulankhula ndi Yesu kwambiri kotero kuti anali kufuna kucita mosutsana ndi maganizo a oweruza ena.

Pa Marko 10:17 Buku Lopatulika linena kuti iye anathamanga kupita kwa Yesu. Ici ndi cithuncithunzi ca munthu wacuma cambiri kuthamanga kupita kwa munthu wosowa kwambiri. Ndipo pamene anadza kwa Yesu anagwa pansi pa maso a Yesu. Anthu ena anali kuyang'anitsitsa oweruza wacinyamatayo. Koma iye

kwa Yesu ai. Cinthu ici ca mbalayi citionetsa kuti munthu angathe kupulumuka pa nthawi yotsiliza moyo wace, koma pamene muwelenga Cipangano ca Kale mudzaona kuti ndi mbala yokhayi imene inayembekezera mpaka pa nthawi yakutha moyo wace. Ndi kwabwino kwambiri kupereka mitima yathu kwa Yesu tsopano lino. Yesu afuna kuti ife tikhale ndi moyo wotsata za Iye tsiku ndi tsiku la moyo wathu, osati nthawi yokha imene tidziwa kuti moyo wathu uli kutha.

4. Yesu anafa pa mtanda cifukwa ca macimo athu. Anafa kukhala ngati nsembe yathu. Anafa kuti onse amene akhulupilira mwa Iye akakhale ndi moyo wosatha ndi Iye. Munthu woyamba kulowa kumwamba cifukwa ca mtanda anali mbala ija imene inafa pa mtanda paja.

MAFUNSO:

1. Kodi munthu ayenera kucita ciani kuti apulumutsidwe?

2. Kodi munthu angathe kupulumutsidwa popanda ubatizo?

3. Kodi munthu ayenera kusanduka mkristu nthawi iti?

-ooOoo-



anthu kuti Bartimeyu adze kwa Iye. Munthu wina amene anali m'khamu la anthuwo anadza kwa Bartimeyu nati, "Limba mtima, nyamuka, akuitana."

Bartimeyu anadzidzimuka ndi kugunda mtima ndipo anasiya cobvala cace pansi. Pamene anali kuperekedwa kwa yesu mtima wace uyenera kukhala kuti unali wosangalala kwambiri. Pamene anamva Yesu ali kulankhula, "Ufuna kuti ndikucitire cinai?" Bartimeyu anayankha mwamsanga, "Ndifuna kuti Inu mucilitse maso anga, ndifuna kuona."

Yesu anamuyankha nati, "Cikhulupiliro cako cakupulumutsa iwe." Ndipo Baritmeyu anatsegula maso ace ndipo cinthu coyamba kuciona cinali nkhope ya Yesu.

MAPHUNZIRO

1. Mwa Baritmeyu tiona munthu amene ali wofuna kubvomera cimene iye anacisowa kwambiri pa moyo. Sianthu onse amene abvomera zosowa zao. Kuposa zinthu zina zonse iye anafuna kuti maso ace atsegulidwe. Anthu amuna afuna kuona zosowa zao. Kukhululukidwa macimo ndico cinthu cacikuru kwambiri cimene anthu afuna kupeza. Koma Yesu sangathe kutithandiza ngati sitifuna kubvomereza zosowa zathu.

2. Ngakhale kuti maso ace a thupi la nyama a Bartimeyu anali akhungu, maso a mtima wace nthawi zonse anali wotseguka. Anali wosiyana ndithu ndi Afalisi. Anali kuona ndi maso ao a thupi la nyama, koma maso a mitima yao anali akhungu. Sanali kuona ndi maso ao a uzimu. Yesu anati, "Muli ndi maso, koma simuona." Koma kwa Baritmeyu, iye analandila kuona kwa maso a thupi la nyama cifukwa anali ndi kuona kwa uzimu.

3. Aliyense amene aitana kwa Yesu kuti apeze thandizo adzamumvera. Khamu la anthu lija linafuna kuti Bartimeyu akhale cete. Kapene anali kuyesa kukhala ndi cifundo pa Yesu. Koma sitingakhale ndi cifundo pa Yesu ngati tilibe cifundo kwa anthu anazathu amene Iye anawalenga. Yesu siacoka pamene munthu alira kufuna thandizo. Ngati timuitana Iye adzatimvera.

4. Mwai woyamba umene Bartimeyu anali nao wakuitana Yesu unalinso mwai wotsiliza umene anali nao. Iyi inali nthawi yotsiliza imene Yesu anadzera kupyola Yeriko. Ici cingakhalenso coona kwa anthu ambiri lero lino. Buku Lopatulika litiuza kuti, "Lero ngati mudzamva mau anga musaumitse mitima yanu." Ahebri 3:7-8. Ngati tili ndi mwai woitana kwa Yesu ndipo tilephera kuitana, mwina mwai wotero sudzabweranso.

5. Yamikani Mulungu cifukwa ca munthu amene anauza Bartimeyu kuti Yesu anali kupita m'njira. Pamene Bartimeyu anagwira cobvala ca munthuyo munthu ameneyu akanakana ndi kumkankha Bartimeyu osamuuza iye za Yesu. Koma munthuyo anaima kanthawi ndipo anauza Bartimeyu kuti Yesu anali kupita m'njira. Yesu ali kupitanso m'mizinda yathu ndi m'midzi yathu. Kodi mwauzako munthu wina ali yense kuti Yesu ali mumzinda mwanu? Mulungu afuna kuti inu mutero.

MAFUNSO:

1. Pafupi ndi Yesu, muganiza kuti pali munthu uti amene ali wofunika kwambiri mu cozizwitsa ici?
2. Kodi munauzako munthu wina ali yense kuba Yesu ali kupita njira?
3. Kodi mwathandizpao wina kuti adze kwa Ambuye Yesu?



Panangopita kanthawi pang'ono pamene Yesu analankhula ndi mbalayo ndipo Yesu anafa. Yesu anafa anthu akubawo asanafe. Koma sipanapite nthawi yaitali Yesu atafa kuti mbala ina ija inafa. Ndipo atafa mzimu wace unapita kumwamba. Pamene adalowa kumwamba Yesu anakomana naye. Mfumu inalowa mu Ufumu wace ndipo inakumbukira mbala ya pa mtanda ija.

MAPHUNZIRO:

1. Zimene zinacitika ndi mbala ija pa mtanda paja zitsimikizira kuti kulapa kokha ndi cikhulupiliro cokha ndizo zili zofunika pa cipulumutso. Munthu uyu sanabatizidwa. Ngati kunali kofunika kuti munthu abatizidwe kuti akhululukidwe, mbala iyi siikanakhala ndi cikhululukiro ca Mulungu. Sanacite nchito yabwino ndi imodzi yomwe. Analijkufa. Analibe mwai wopita ndi kuonetsa kwa ena kuti iye analapa. Cimene anatha kucita ndico kukhulupilira mwa Ambuye Yesu Kristu. Ndipo cifukwa ca kulapa kwace ndi cikhulupiliro cace iye anapeza cipulumutso.

2. Munthu ali yense asankhe yekha ngati afuna kaya safuna kubvomera macimo ace ndi kutsata Yesu. Panali mbala ziwiri zimene zinafa pa mtanda paja. M'modzi wa iwo anakhulupilira mwa Yesu, ndipo wina sanakhulupilira. Wina wa iwo anapita kumwamba, wina wa iwo anapita ku gahena. Munthu ali yense atsimikize mtima ngati afuna kukhala wotsatira wace wa Yesu.

3. Mbala pa mtanda paja anasanduka mkristu, ana sanduka mkristu asanafe. Ici sicitanthauza kuti anthu ayenera kuyembekezera mpaka nthawi imene moyo wao uli pafupi kutha asanabwere kwa Yesu. Ici sicitanthauza kuti munthu ayenera kulindira nakhala osapereka mtima wace

Mfumu." Ansembe akuru-akuru ndi alembi anamuyang'-ana Iye ndipo nanena kuti, "Unapulumutsa ena, bwanji osadzipulumutsa wekha?" Nkobvuta kuzindikira cifukwa ciani analankhulila mau otere kwa Yesu. Moyo wace wonse anakhala ali kucita zabwino. Anacilitsa wodwala. Anatsegula maso a anthu wosaona. Ndi Yesu yemweyu amene uja anakonza munthu wakhate uja. Koma tsopano pamene anali kufa khamu lonse linaiwala zinthu zonsezi.

Pa nthawi yomweyo mmodzi wa mbala zimene zinapacikidwa pamodzi ndi Iye anayamba kulankhula. Anafuna Yesu kuti agwiritse nchito mphamvu yace kuti awatsitse pa mtanda paja. Koma mbala ina inathandiza Yesu. "Ife tili kufa cifukwa ca nchito zathu zoipa zimene tinacita, munthu uyu sanacimwa. Ali kufa cifukwa ca nchito zabwino zimene Iye anacita."

Pamenepo mbala pamtanda paja inati kwa Yesu, "Mundikumbukire mmene mulowa Ufumu wanu." Anatembenuka mtima. Analeka macimo ace napempha Yesu kuti amukhululukire. Kumva cisoni cifukwa ca macimo athu sikutanthauza kuti tili kulapa. Kulapa kutanthauza cinthu coposa kungokhala ndi cisoni. Anasintha maganizo ace nidpo Yesu anasintha mtima wace.

Ncodabwitsa kuona kuti mbala ija inaganizira kuti Yesu anali Mfumu. Yesu anali kufa pa mtanda Anaitana pa Yesu mwa macitidwe a cikhulupiliro. Mbala iyi inali kuitana Yesu pa nthawi yace ya kufa kupempha Yesu kuti alowe mumtima mwace.

Yesu anayankha pa cikhulupiliro ca mbalayo. "Lero lino udzakhala ndi Ine m'Paradaiso." Yesu anakhululukira macimo ace nalonjeza kwa mbalayo kuti adzapita ndi Iye kumwamba. Ambanda, Mbala ziwiri zija sizinali ngati mnzaoyu tsopano. Awiri amenewa anakhalabe m'moyo wao waucimo koma anali osiyana ndi poyamba paja tsopano. Mbala imodzi inapitilirabe kuseka Yesu --- koma winayo anakhulupilira mwa Iye.



PHUNZIRO 2

## YESU NDI MUNTHU WODWALA MANJENJE

MAU A MULUNGU: Mateyu 9:1-8; Marko 2:1-12; Luka 5: 17-26.

MAU A PA MTIMA:

"Ndipo Yesu pakuona cikhulupiliro cao ananena ndi wodwala manjenje, Mwana, macimo ako akhululukidwa."

Marko 2:5.

### MBIRI YACE

Iyi ndi imodzi ya mbiri zodabwitsa kwambiri m'Buku Lopatulika. Itionetsa ukuru wa mphamvu ya Mulungu ndi cikhululukiro ca Mulungu. Tiyene tionetsetse cithunzithunzi cace cimene ndime izi zitipatsa.

Yesu anali kuphunzitsa mu Kapernao. Anali kuphunzitsa m'nyumba ina m'Kaperano. Anthu ambiri anadza kudzamva za Iye. Abwenzi ace pamodzi ndi adani ace anali kumeneko. Nyumba inadzaza kwambiri ndi khamu la anthu kotero kuti panalibe wina amene akanatha kulowamo. "Panali Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo, amene anacokera ku midzi yonse ya ku Galileya ndi Yudeya ndi Yerusalemu." Luka 5:17.

Pamene Yesu anayamba kuphunzitsa ndi kulankhula ndi anthu tsindwi (denga) linayamba kucoka. Munthu wina anakwera pa dengapo. Anthu a m'nyumbamo anayamba kuyang'ana kumwamba kwa nyumbayo kuti aone cimene cinali kucitika. Ndipo posacedwa anthu a m'nyumbawo anaona kuti panali anthu anai pa dengapo. Anayesa kudzera pakhomo, koma khamu la anthu

silinawalore kupyolapo. Anthu anai awa anafuna kwambiri kuona Yesu. Anatsimikiza mtima. Palibe cimene cikanawaletsa.

Anafuna kuona Yesu cifukwa ca mnzao. Anali wodwala kwambiri. Thupi lace lonse linali kunjenjemera. Sanali kutha kuyenda. Anali wodwala kwambiri kotero kuti anali kukhala pa mphasa pace nthawi zonse. Anali kudwala nthenda ya manjenje.

Pamene anazacewo anaboola pa tsindwipo, anthu onse amene anali m'yumbamo anadabwa kwambiri. Anthu sanazindikira cimene cinali kucitika. Pamenepo anzace anaiwo anayamba kutsitsa mphasa yace kudzera pamene anaboolapo. Anatsitsa mphasa yaceyo pang'ono-pan'ono. Ndipo mwamsanga, pa mapazi pa Yesu panali kugona munthu wodwalo manjenjeyo. Ho, munthu wacisoni nanga kumuona. Anali munthu wamng'ono amene thupi lace linadzaza ndi matenda.

Pamene Yesu anaona munthu wamng'onoyo anati, "Mwana, khala wosangalala," Mateyu 9:2. Ndipo pa Marko 2:5 Yesu anati, "Mwana, macimo ako akhulukidwa." Ndipo cinthu cacitatu cimene Yesu ananena kwa iye cinali ici, "Tauka, nusenze kama wako, numuke ku nyumba kwako." Luka 5:24.

Pamene Yesu anauza munthu uja kuti akhale "wosangalala", anali kumuuza munthuyo kuti asaope. Ndipo, pamene anayang'ana m'maso mwa mnyamata wodwalayo, Yesu anati, "Macimo ako akhululukidwa." Pamene anthu anzeru anamva Yesu alikunena mau amenewa anadabwa. Anayamba kulankhulana wina ndi mnzace. Ndipo iwo anati, "Palibe wina angathe kukhululukira macimo koma Mulungu. Kodi munthu uyu aganiza kuti ali Mulungu?" Yesu anadziwa maganizo ao. Anadziwa cimene cinali kuwabvuta. Ndipo pamene anatembenukira kwa iwo anati, "Kodi capafupi nciti,



PHUNZIRO 12

## YESU NDI MBALA PA MTANDA

MAU A MULUNGU: Mateyu 27: 1-66; Marko 15: 1-47; Yohane 19-1-41; Luka 23: 39-43.

MAU A PA MTIMA:

"Ndipo iye ananena kwa Yesu, Ambuye, ndikumbukireni pamene mulowa Ufumu wanu."
Luka 23: 42.

### MBIRI YACE

Mbiri ya mbala yakufa pa mtanda ndiyo mbiri yodabwitsa ya cikondi ca Yesu. Iyi ndiyo mbiri yotsiliza imene tili nayo ya munthu wakudzipereka yekha kwa Ambuye Yesu asanafe pa mtanda.

Inali nthawi yakuti Yesu anali yekha pamene ananka ku mtanda. Akuphunzira anamusiya nathawa. M'modzi wa iwo anampereka Iye. Wina anamkana Iye. Ndipo ena siachulidwanso pamene Yesu anapita kukafa pa mtanda. Pamene anapacikidwa kufa cifukwa ca macimo athu Iye sadayang'anenso nkhope za abwenzi. Anayang'ana nkhope za iwo amene anali wosangalala pakumuona Iye ali kufa. Anali kumuseka Iye. Anamutsira malobvu. Anacita cili conse cimene anatha kucita pakufuna kuti amve kuwawa kwambiri.

Njira yaululu wambiri pakufa kwa munthu inali pakufa pa mtanda. Asilikali anakhomera misomali m'manja ndi m'mapazi a Yesu, anaika korona wa minga pa mutu pace, ndipo anamumenya. Tsopano anali kuyembekezera kuti afe. Anthu amene anali kupita m'njira nayang'ana kwa Yesu anati. "Ha, Iwe unati ndiwe

ku Gadara anamuuza Yesu kuti acoke, Yesu anali ndi mbonibe m'mudzimo.

3. Anthu a ku Gadara anamuuza kuti acoke m'mudzi mwao. Sanafuna kuti Iye akhalemo cifukwa nkhumba zao zinafa. Pali coopsa pakuuza Yesu kuti acoke. Pamene mumuuza Yesu kuti acoke Iye adzacokadi.

MAFUNSO:

1. Kodi mizimu yoipa ingagonjetsedwe bwanji?

2. Kodi Yesu ayembekezera kuti mkristu ali yense acite cinni?

3. Coopsa ndi ciani pakuuza Yesu kuti atisiye ife tokha?

-ooOoo-



kunena, Macimo ako akhululukidwa; kapena kunena, Tauka, nuyende?" Apa anali kunena kuti Mulungu yekha ndiye angakhululukire macimo ndi kucilitsa.

Pamene anatenbenukira kwa mnyamata wodwala manjenjeyo Yesu anati, "Tauka, yalula mphasa yako nuyende." Ndipo mwamsanga anaimilira. Anacilitsidwa. Nthenda inacoka. Ananyamula kama wace namuka ku nyumba kwace alikuyamika Mulungu cifukwa ca zonse zimene anamucitira iye. Ndipo anthu analankhulana wina ndi mnzace nati, "Taona zinthu zacilendo lero."

MAPHUNZIRO

1. Mu ndime izi zimene taphunzira lerozi tiona cimene citanthauza pakukhala bwenzi leni leni, loonadi. Buku Lopatulika litiuza ife kuti munthu wodwala manjenje uja ananyamulidwa ndi abwenzi anai kufika naye kwa Yesu. Pamene anafika ku nyumba kumene Yesu anali kuphunzitsa napeza kuti nyumba inali yodzaza ndi anthu iwo anataya mtima, koma osada nkhawa. Analimba mtima. Panalibe cina cowaletsa. Anali ndi cofuna cimodzi. Anafuna kufika kwa Yesu ndi bwenzi lao uja. Bwenzi lao anali kusowa cinthu cimene wina aliyense sakadamupatsa koma Yesu. Anthu anai awa anali anthu acikhulupiliro cacikuru. Sanada nkhawa ndi zobvuta.

2. Cikondi copanda nchito sicikondi. Ngati tili ndi cikondi ca Yesu m'mitima mwathu tidzapitilirabe ngakhale pamene nchito yathu yaima. Cikondi ca pa Yesu m'mitima mwathu cionekera pa zinchito zathu, osati m'mau athu okha. Abwenzi anai aja anamukonda kwambiri munthu wodwala uja kuti iwo sanalephera mpaka Yesu anamucilitsa iye.

3. Cipembedzo ca Cikristu ciuza antu cinthu cina cimene cipembedzo cina sicingawauze iwo. Cipembedzo ca Cikristu cokha ndico cimene cingathe kuuza anthu za cikhululukiro codabwitsa ca Mulungu. Zipembedzo zina zonse ziuza anthu kuti agwire nchito kwambiri ndi kucita zabwino ngati afuna kuti adzaone Mulungu. Koma m'cipembedzo ca Cikristu Mulungu atsika mwa Mwana wace Yesu Kristu ndipo auza anthu onse kusiya zoipa zao ndipo Mulungu adzawakhululukira. Uthenga wa Yesu ndiwo uthenga wacikhululukiro ca macimo.

4. Pali phunziro lina lakuti tiphunzirepo kucokera pa munthu wodwalayu. Abwenzi ace atacita zonse zimene anakhoza kucita, ndipo Yesu atacita zonse zimene anatha kucita, cinali kwa wodwalayo kucita cimene akanakhoza kucita. Wodwalayo akanaonetsa ngati anali ndi cikhululupiliro cokwanira kuti ayende.

5. Pali phunziro linanso. Ili ndi phunziro lalikuru kwambiri. Liwelengeni bwino bwino. Kodi zikadakhala bwanji ngati munthu uja anagwa pansi pamene anali kuyesa kuimilira kuti ayende? Kodi zikadakhala zotani ngati munthu uja akadayesa kuyenda koma miyendo yace nkukhala yosayenda? Sili phunziro lace ------ Yesu anadzitsimikizira kwathunthu kuti Iye ndiye Mwana wa Mulungu pamene munthu uja anakhoza kuyenda. Ndipo wodwala uja anakhazika ciyembekezo cace conse pa Yesu. Cili cimodzimodzi ndi miyoyo yathu. Ngati tifuna kudziwa mphamvu ya Mulungu m'miyoyo yathu tiyenera kukhulupilira kuti cili conse cili cotheka ndi Iye.



yonyansa. Mankhwala siangathandize. Mfiti sizingathandize. Yesu yekha ndiye ali ndi mpahmvu yocotsa mizimu yonyansa m'miyoyo yathu. Pamene Yesu alowa mumtima mwathu amadzaza mitima yathu ndi Mzimu wace. Amadzaza mtima wathu ndi mzimu woyamika ndi wa cimwemwe. Pamene Mzimu wa Yesu uli m'mitima yathu mpahmvu ya mzimu wonyansa yacoka.

Pamene anthu a m'mudzi wa Gadara anadza kudzaona Yesu anaiwala zonse za munthu uja amene anali wogwidwa ndi mzimu wonyansa. Anabwera ndi cidani m'mitima yao cifukwa Yesu anali ndi mphamvu yoposa yao. Anaturutsa mizimu yoipa. Analora mizimu yoipayo kulowa m'nkhumba. Cifukwa ca cimeneci anthu aja anafuna kuti Yesu acoke. Anacita misala cifukwa anataya cuma cao. Akanayenera kukhala wokondwera cifukwa mnzao anacilitsidwa.

MAPHUNZIRO

1. Cili cinthu comvetsa cisoni kwambiri kuona anthu ali wogwidwa ndi mzimu woipa. Pali njira imodzi, imene tingawathandize nayo. Tingathe kupempherera Mzimu wa Ambuye Yesu kuti ulowe m'mitima yao ndikuwadzaza ndi Mzimu wace.

2. Atacilitsidwa munthu wa ku Gadara uja anafuna kutsata Yesu. Koma Yesu anali ndi njira ina. Anamuuza kuti abwerere kupita ku mudzi kuja ndi kuuza anthu cimene Mulungu anamucitira. Yesu anafuna kuti iye abwerere ku mudzi kukacitira umboni kwa anthu amene anali m'mudzi wa Gadara. Ici ndico cimene Yesu ayembekezera kucitidwa ndi onse amene abvomereza kuti ndiye Mpulumutsi wao. Mkristu ali yense ayenera kukhala mboni. Pamene Yesu adza kukhala m'mtima mwathu afuna ali yense wa ife kuuza abwenzi athu ndi anansi athu za Iye. Ngakhale kuti anthu a

njira zambiri koma analephera kumupanga iye kuti akhale cete. Usana onse ndi usiku onse anali kukhala m'mapiri ndi m'manda kulira ndi kudzicekaceka yekha ndi miyala.

"Koma pamene iye anaona Yesu." Awa ali mau odabwitsa. Pakuti Buku Lopatulika linena kuti pamene iye anaona Yesu anathamanga ndi kumpembedza Iye.. Pamene anafika ku malo amene Yesu anaimilirako Yesu analamulira ziwandazo kuti zituluke mwa munthuyo. Pamene mizimu yonyansa inaturuka mwa munthu wa ku Gadara inalowa m'nkhumba. Nkhumba zinacita misala cifukwa ca mizimu yonyansayo ndipo zinathamanga kutsika m'phiri lotsetsereka ndi kulowa m'nyanja.

Tsopano Yesu anali kuyang'ana kwa munthu wa ku Gadara, koma munthuyo anakhala wosiyana ndi poyamba paja. Sanalinso wamisala. Anakhalanso bwino. Anthu sadayenerenso kumuopa iye. Akuphunzira a Yesu anamupatsa nsaru kuti akute thupi lace. Ndipo pamene mwini wace wa mkhumba anadza kudzadandaula kwa Yesu, munthu wamisalayo anakhala tsonga ali obvala. Komatu, eni ace a nkhumba zija sadamuona iye. Anali wokwiya cifukwa nkhumba zao zinafa. Munalibe mayamiko mumtima mwao cifukwa cakuti wamisala anali bwino. Cili comvetsa cisoni kwambiri pamene anthu akonda zinthu kwambiri kotero kuti siatha kuona madalitso a Mulungu. Adayenera kubwera kwa Yesu kudzamuyamika Iye. Adayenera kubwera kudzamuyamikira Iye cifukwa cakucilitsa bwenzi lao. Koma, ai. Anali ndi cidwi cambiri munkhumba.

Anthu ambiri ali ndi mafunso pa za mizimu yonyansa. Kodi mizimu yonyansa imakhaladi ndi anthu? Buku Lopatulika likuti inde. Pamene munthu akhala ndi mizimu yonyansa citanthauza kuti mizimu yonyansayo ili ndi mphamvu pa moyo wa anthuwo. Yesu yekha ndiye amene angathe kuthandiza munthu amene ali ndi mizimu



MAFUNSO:

1. Mwacita ciani kuthandiza abwenzi anu kuti apeze Yesu Kristu?

2. Kodi mwauzako bwenzi lanu lina mmene inu munakhululupilira Yesu monga Mpulumutsi wanu?

3. Muganiza kuti cacikuru kwambiri ndi citi pa cozizwitsa ici?

-ooOoo-

PHUNZIRO 3

## YESU NDI MKAZI WACIGOLOLO

MAU A MULUNGU: Yohane 8: 1-11.

MAU A PA MTIMA

"Amene mwa inu ali wopanda cimo, ayambe kumponya mwala."

Yohane 8:7.

### MBIRI YACE

Yesu anali kupemphera ku phiri la Azitona. Atatha kupemphera mmamawa anankanso ku Kacisi. Pamene anthu anamuona anayamba kusonkhana momzungulira Iye. Pamene Yesu anaona cidwi cao, anakhala pansi ndipo anayamba kuwaphunzitsa. Pamene Iye anali kuphunzitsa anthu anamvetsera mwacete. Anafuna kumva mau ali onse amene Iye analankhula.

Pamenepo, mwadzidzidzi, anthu anayamba kuyenda mopitilira anafuna kufika kutsogolo kwa Yesu. Anthu awa sianali abwenzi ace a Yesu. Anayesetsa kuletsa anthu kuti asamvere zonena za Yesu. Ena anali alembi ndipo ena a iwo anali kuchedwa Afarisi. Mlembi anali ndi nchito ziwiri. Pa gawo lina anali kukhala ophunzitsa malamulo a Cipangano ca Kale kwa anthu. Alembi sianali abwenzi a Yesu ndipo a nayesetsa kuutsa cobvuta pa Iye. Afarisi ndiwo anali atsogoleri a Cipembedzo pamene Yesu anadza kudzakhala pa dziko lapansi. Anali ndi malamulo ambirimbiri. Anakhulupilira kuti cinthu cacikuru kwabiri cinali kutsata malamulo a Cipangano ca Kale. Sanatsata Yesu ndipo sanaonetsa cikondi kwa anthu ena. Alembi awa ndi Afarisi ndiwo amene anali kukankha m'khamu la anthu kuti apyole kufika kwa Yesu.



PHUNZIRO 11

## YESU NDI MUNTHU WA KU GADARA

MAU A MULUNGU: Mateyu 8:28-34; Marko 5:1-20; Luka 8:26-39.

MAU A PA MTIMA

"Pakuti ananena kwa iye, Turuka iwe, mzimu wonyansa kwa munthuyu."

Marko 5:8.

### MBIRI YACE

"Pamenepo munthu wogwidwa ndi mzimu wonyansa anakomana ndi Yesu, munthu uyu anali kukhala ku manda --- masiku onse usiku ndi usana, m'manda ndi m'mapiri, anali kulira, ndi kudzicekaceka yekha ndi miyala." Mateyu anena kuti anali wamisala ndipo anali kuopsa anthu. Luka anena kuti munthu ameneyu sanali kubvala zobvala. Mau awa afotokozera za wa ku Gadara. Munthu wodzala ndi mzimu woipa.

Yesu ndi akuphunzira ace ndiye atangooloka nyanja kufika pa tsidya lina m'kangalawa kwa kakangono. Pamene anali kuturuka m'ngalawa munthu wooneka moopsa anadza ndi liwilo kulunjika kwa iwo. Anali wamarisece. Thupi lace linali la ubve kwambiri. Anali ndi mabala m'manja ndi m'miyendo yace yonse. Cinali comvetsa cifundo kuona munthu wotero. Anali kukhala m'manda. Anthu a m'mudzi sanamulora iye kukhala m'mudzi pamodzi ndi anthu ena. Iwo anayesetsa kucitapo kanthu pakumsunga munthu uyu. Kumuletsa kuti asamaopse anthu anamumanga ndi maunyolo. Koma mzimu wonyansawo unamupatsa mphamvu zambiri kotero kuti anali kukhoza kudula unyolowo. Anthu anayesa

2. Pamene Yesu anaciritsa thupi la munthu uja, munthuyo sanadziwa kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Anangodziwa kuti thupi lace linaciritsidwa. Atacilitsidwa malo oyamba amene iye anafuna kupitako anali ku Kacisi kukayamika Mulungu. Mtima wace unakondwera kwambiri. Anafuna kupemphera. Anafuna kuti Mulungu adziwe cimwemwe cimene anali naco mumtima mwace. Anthu onse siacita cimeneci. Mulungu amacilitsa anthu ambiri, koma sionse amene amyamika Mulungu cifukwa ca kuwacilitsako.

3. Kubvutika kwa munthu uyu kunadza cifukwa ca chimo la iye mwini. Iye anasankha kucita chimo ndipo cimo linapundula thupi lace. Ndi cofunika kwambiri kwa ife kusunga malamulo a Mulungu. Munthu amene akondadi Yesu sangakhale wosangalala kuti akhale mu ucimo. Chimo nthawi zonse limapundula.

4. Yesu atangocilitsa munthu uyu anamuuza kuti acokepo pa malopo pamene anakhalapo zaka makumi atatu kudza zisanu ndi zitatu. Yesu anauza munthuyo kuti asiye moyo wakale ndi malo akale. Anapita ku malo atsopano kumene Mulungu anafuna kuti iye awapeza. Ndi cimodzimodzi pamene tisanduka akristu. Pamene tipereka mtima wathu kwa Yesu tisanduka "olengedwa atsopano". Monga wokhulupilira atsopano Yesu afuna kuti tisiye malo akale a ucimo ndi kukhala ndi Iye m'nyumba ya Mulungu.

MAFUNSO:

1. Cifukwa ciani munthu uyu anali wopunduka?

2. Yesu anamuuza ciani munthuyu pamene anamucilitsa?

3. Kodi cinthu coyamba cimene munthuyu anacita atacilitsidwa nciani?



amene anali kukankha m'khamu la anthu kuti apyole kufika kwa Yesu.

Koma sianali okha. Pamene anafika pa malo amene Yesu anali kuimilirapo kutsogolo kwao anali kukankha mkazi amene anali wamarisece. Pamene anafika pa malo pamene anaimilira Yesu iwo anakankha mkaziyo kuti afike kutsogolo kwa Yesu. Khamu la anthu silinazindikira zimene zinali kucitika. Kodi anthu amenewa anali kufuna kucita ciani? Anali kuyesa kumulakwitsa Yesu pa maso pa khamu la anthu. Anali kuyesa kumufunsa funso limene Iye sakanatha kuliyankha.

Munthu ali yense anamvetsera pamene Afarisi anayamba kulankhula. Anali kuuza Yesu cifukwa cimene anadzera kwa Iye ndi mkazi uja. "Mkazi uyu", iwo anatero, "Wapezeka m'chimo la cigololo." "Muganiza kuti ticite ciani ndi iye?"

Afarisiwo anali a Yuda. Anali kukhala mosunga malamulo a Mose. Anthu ambiri amene anali kumvetsera kwa Yesu analinso a Yuda. Ngati Yesu akadanena kuti mkaziyo amuleke ndipo amulole kuti apite ndi ufulu wace Iye akadaphunzitsa cosiyana ndi lamulo la Mose. Levitiko 20:10. Koma Ayuda anali kukhala pa ulamuliro wa ciRoma. Ndipo lamulo la ciRoma linanena kuti asaphe munthu wina ali. yense. Comweco iwo anaganiza kuti cili conse cimene Yesu akanayankha iwo akanautsa naco bvuto pa Iye. Alembi ndi Afarisi aja sianali ndi cidwi kweni kweni ndi mkazi uja; iwo anali ndi cidwi pakuutsa bvuto pa Yesu.

Yesu sanawayang'ana iwo. Yesu anawelama pansi ndipo analemba pa mcenga ndi cala cace. Mtima wace unali ndi cisoni cambiri cifukwa ca macitidwe a alembi ndi Afarisi. Iye nadodomanso cifukwa ca mmene iwo anacitira ndi maiyo. Pamene anali kugwada pansi iwo anamufunsa kawiri kawiri, "Utiuza kuti ticite ciani?"

Lamulo la Mose linanena kuti mkazi wopezeka ndi cigololo aponyedwe miyala ndi kuphedwa. Yesu anadziwa za lamulo ili, ndipo Afarisi aja anadziwa za lamuloli. Ali yense anali kuyembedezera kumva yankho la Yesu kwa alembi ndi Afarisi. Ndipo tsopano anali pafupi kuti ayankhe. Asanawelemuka mutu wace Yesu anati, "Amene alibe chimo ayambe kumponya mwala." Yesu anadziwa cimene Afarisiwo anali kucita, Anafuna kuweruza munthu wina, koma sanafuna muntu wina kuweruza iwo. Yesu anadziwa mitima yao. Anadziwa chimo lao. Afarisi aja anafuna kuyang'ana ku chimo la mkazi lija. Sanafuna kuyang'ana ku chimo lao.

Yesu atatha kuyankha funso lao alembi ndi Afarisi anayamba kucoka. Pamenepo Yesu anayang'ana kwa mkaziyo nati, "Ali kuti anthu aja anakuweruza iwe?" Ndipo mkaziyo anati, "Ambuye, acoka palibe." Sanathe kumuweruza mkazi uja pamene Yesu anawayankha funso lao lija. Pamenepo Yesu anati kwa mkaziyo. "Inenso sindikutsutsa iwe: pita; ndipo usakacimwenso." "Yesu anamukhululukira mkazi uja ndipo anamupatsa mtendere.

MAPHUNZIRO

1. Pa umodzi wathu wa ife ndi ena sitiyenera kuweruza. Mulungu ndiye oweruza. Yekha amene alibe chimo ndiye ayenera kuweruza. Mulungu afuna kuti ife tionetse cikondi cace kwa anthu onse. Tisathe nthawi yathu pakuweruza ena.

2. Ncapafupi kufuna kuti anthu ena acite cinthu cabwino pamene ife tilephera. Alembi ndi Afarisa aja anali kuyembekeza kuti mkazi uja aphedwe. Koma munthu amene anacita cigololo ndi mkaziyu anali kuti? Mulungu anangopereka malamulo. Malamulo a Mulungu sasiyanitsa pakati pa anthu.



Pamenpo Yesu anati "Yenda". Ndipo malo woyamba kuyendako anali ku Kacisi. Anapita kwa Mulungu. Sanadziwa kuti Yesu anali yani. Ndipo pamene anthu anamufunsa kuti ndani anamuthandiza iye analephera kuyankha. Sanadziwa. Koma anadziwa kuti iye mwini anafuna kuyamika Mulungu cifukwa ca thupi lace lamphamvu ndi latsopano.

Anali m'Kacisibe pamene Yesu anadza kwa iye nthawi yaciwiri. Ndipo Yesu anati kwa iye, "Taona, waciritsidwa; usacimwenso, kuti cingakugwere coipa coposa."

"Usacimwenso kuti cingakugwere coipa coposa ici." Yesu anatero. Pa limodzi la maphunziro athu ena tinaphunzira za cimo ndi kumva zowawa. Tinaphunzira kuti kumva zowawa konse kumene kuli pa dziko lapansi kunadza cifukwa ca chimo la munthu. Tinamvanso kuti osati titangoona munthu ali kumva zowawa ndiye kuti nthawi zonse citanthauza kuti munthuyo ali kubvutika cifukwa ca chimo lace ai. Koma pano, Yesu anena momveka bwino kuti munthu uyu anamva zowawa cifukwa ca macimo amene anawacita. Ndico cifukwa cace cimene Yesu anamuuzira munthu uja kuti asabwererenso ku malo a zowawa. "Yalula zofunda zako nuyende." Ici ndico cimene Yesu atiuza ife pamene adza mumitima yathu kuti akhalemo.

MAPHUNZIRO

1. Yesu Kristu afuna kuti akhale bwenzi la munthu ali yense. Kwa Iye zilibe kanthu ngati anthu alibe abwenzi. Yesu adza kwa ife natiitana kuti tisiye macimo athu ndi kulapa. Atiitana ife kuti tidze mwa cikhulupiliro kwa Iye ndi kulora Iye kuti akhululukire ife. Pamene Yesu anaona munthu uyu sanaime kutali ndi iye. Anapita pafupi ndi iye. Anamuthandiza..

munthuyo anayenda nafika pafupi ndi iye nati, "Ufuna kuti thupi lako licitsidwe ndi kukhalanso la mphamvu kodi?" Munthuyo anayang'anitsitsa Yesu nati, "Bambo, ndifuna kwambiri kuti thupi langa licilitsidwe, koma ndilibe wakundibviika m madzi." Awa ndi malo omvetsa cisoni. Ndi cithunzithunzi ca munthu amene siali wopunduka kokha, koma ali munthu opanda abwenzi.

Apa panali munthu wosowa thandizo. Munthu amene analibe ciyembekezo cifukwa analibe thandizo. Koma Yesu anamuuza kucita cinthu cimodzi cimene sakanatha kucita. Anamuuza kuti anyamuke nayende. Anamuuza kuti atenge zofunda zace ndi kuyenda. Kawiri kawiri Yesu atipanga ife kuti tiyang'ane ku zinthu zimene tiganiza kuti sitingacite ndipo pamenepo atiuza ife kuti ticite zinthuzo. Kodi zimenezi zimacitika bwanji?

Yesu anafunsa munthuyo ngati anali kufuna kuti ayende. Ici ndico cinali cinthu cimodzi cimene munthuyo anafunitsitsadi kuti acicite. Pa zaka makumi atatu kudza zisanu ndi zitatu iye anakhala ali kufuna kuyenda. Yesu anafunanso kuti munthuyo ayende. Ndipo pa nthawi yomweyo pamene cifuniro ca munthuyo cinakhudzana ndi cifuniro ca Mulungu mwa Kristu, mphamvu yakucilitsa inabwera ndipo munthu wopundukayo anakhoza kuyenda.

"Yalura mphasa yako." Yesu anatero. Cifukwaninji Yesu anafuna kuti munthuyo atenge mphasa yace? Iye anafuna kuti munthu uja atenge mphasa yace nacoke pa malo pa zowawa pamene anakhalapo nthawi yaitali. Sanafuna kuti munthu uja abwererenso ku malo kumene anakhalako nthawi yaitali. Anafuna kuti iye apite ku malo atsopano ndipo amtundu wina. Sanafuna kuti munthu uja aceuke.



3. Yesu akonda wocimwa --- koma adana ndi cimo. Pamene aliyense anafuna kuweruza mkazi uyu Yesu anamuchinjiriza. Sadamuuze mkaziyo kuti sadacimwe. Sadamuuze mkaziyo kuti kucimwa kuli kwabwino. Yesu anayang'ana mumtima mwa mkaziyo namuuza kuti asiya cimo lace. Pamene Yesu aitana munthu kucokera ku ucimo pamenepo padza kusinthika mumtima. Yesu anapatsa mkazi uja mphamva yakupambana nayo ucimo. Yesu apatsa wocimwa aliyense amene atembenuka mtima mphamvu yakupambana nayo cimo.

4. Pamene ena onse anafuna kuweruza -----Yesu anafuna kukhululukira. Cikhululukiro ndico pakatikati pace pa uthenga wa Yesu.

MAFUNSO:

1. Kodi Afarisi aja anali kufuna kucita ciani?
2. Kodi cacikuru nciani kwa mkristu ---kuweruza kapena kukonda?
3. Kodi Yesu ananena ciani kwa mkazi uja?

-ooOoo-

## PHUNZIRO 4

## YESU NDI MKAZI WODWALA

MAU A MULUNGU: Mateyu 9:18-26; Marko 5:21-34; Luka 8:42-47.

MAU A PA MTIMA:

"Ndipo Yesu anati kwa mkaziyo, Mwana wamkaziwe, cikhululupiliro cako cakupulumutsa; muka mumtendere, nukhale wocira cibvutiko cako."
Marko 5:34.

### MBIRI YACE

Yesu anali mu Kapernao. Kalenso anapitako kawiri kawiri. Anacilitsa odwala ambiri ndi amatenda ambiri mu Kapernao kale, Ndipo cifukwa kuti anthu akumeneko anadziwa kale za cikondi cace ndi mphamvu yace makamu ambiri a anthu anadza kudzaona Iye.

Pamene anayenda kupyola m'khamulo mmodzi wa atsogoleri a Kacisi wa nyumba ya Mulungu anadza kwa Iye. Dzina lace linali Yairo. Pamene anadza kwa Yesu Yairo anagwa pa mapazi a Yesu. Yairo anali kufuna cinthu cina kwambiri. Ngakhale kuti anali munthu womveka m'mudzimo --- iye anafuna thandizo tsopano limene Yesu yekha ndiye akanatha kumupatsa. Buthu lace linali kudwala kwambiri. Anali pafupi kufa. "Bwerani", anatero Yairo, "ndipo muike dzanja lanu pa iko kuti acile ndi kukhala ndi moyo." Yesu anabvomera kupita ndi iye ndi kuthandiza kabuthu kaceko.

Pamene Yesu anali kuyenda m'njira anthu ambirimbiri anali kuyenda naye. Anali kukankha kuti iwo afike kufupi ndi Yesu. Munali anthu ambiri m'khamumo



## PHUNZIRO 10

## YESU NDI MUNTHU KU THAMANDA

MAU A MULUNGU: Yohane 5: 1-16.

MAU A PA MTIMA:

"Taona, waciritsidwa; kuti cingakugwere coipa coposa."
Yohane 5:14.

### MBIRI YACE

Caka cili conse a Yuda anali kukhala ndi madyerelo ambiri. Pamene Yesu anakomana ndi munthu amene tidzaphunzira za iye lero inali nthawi ya madyerero amodzi a madyerero amenewo. Yesu ananka ku Yerusalemu ku madyereroko.

Panali njira zowelengeka zimene munthu akanathera kulowera m'mudzi wa Yerusalemu. Limodzi la makomowa linali kuchedwa cipata ca nkhosa. Cinali cipata cimene amalonda ambiri anali kulowera. Anali kudzera pa cipata ici cifukwa cinali pafupi ndi malo a msika. Ici ndico cipata cimene Yesu anadzera tsiku limenelo. Pafupi ndi cipata ici panali thamanda la madzi. Madzi a m'thamanda ili anaturuka kucokera pansi. Anthu anali kukhulupilira kuti pa nthawi ina yace madzi awa akanatha kucilitsa munthu pa matenda ace. Cifukwa ca cikhulupiliro ici anthu wopunduka anali kukhala mozungulira thamandalo kuyembekezera nthawi yoyenera kulowa m'thamandalo.

M'modzi wa anthu amene anali kukhala pafupi ndi thamandalo anali munthu amene anali wopunduka kwambiri. Anakhala wopunduka pa nthawi ya zaka makumi atatu kudza zisanu ndi zitatu. Pamene Yesu anaona

anali kuika thope m'maso mwace. Anali wofuna kucita cinthu cili conse ngati cikadamthandiza kuti aone. Koma pamene maso ace anatsegulidwa nakhoza kuona kwa nthawi yoyamba anauza anthu onse kuti Yesu, anatsegula maso ace. Anasanduka wakuphunzira wa Yesu ndipo anthu onse sandtha kusintha mtima wace.

3. Macimo onse autsa kubvutika, koma sitinganene nthawi zonse pamene munthu ali kudwala, kaya amva zowawa m'thupi, kuti ali kubvutika cifukwa ca macimo ao.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi ciani ciutsa zowawa?

2. Kodi Satana amatiletsa bwanji kucita nchito ya Mulungu?

3. Maso ace ataseguIidwa, kodi munthu wosaona uja anacita ciani cimene wakuphunzira ali yense wa Yesu ayenera kucita?

-ooOoo-



motero kuti ophunzira ace a Yesu anadabwitsidwa.

Tsiku limenelo m'khamu la anthulo munali mkazi wina amene anali wodwala kwambiri. Anakhala wodwala pa nthawi ya zaka khumi ndi ziwiri. Anayesetsa nthawi zambiri kuti acilitsidwe. Anapita kwa asing'anga, koma analephera kumucilitsa. Anamwa mankhwala osiyana-siyana koma mankhwalawa sadamuthandiza. Anaononga ndarama zace zonse kuyesa kupeza thandizo. Koma panalibe mmodzi yense amene anamucilitsa. M'malo mopeza bwino matenda ace anali kukulira-kulira.

Pali zinthu zambiri zimene sitidziwa za matenda a mkazi uyu. Komabe, pali zinthu zina zimene tidziwapo za matendawa. M'masiku amene Yesu anali pansi pano, ngati munthu anali ndi nthenda imeneyi anali kuchedwa wonyansa. Anali matenda akurudi. Panali lamulo lakuti ngati mkazi adwala nthenda imeneyi mwamuna wace asakhale naye. Lamulo linali lakuti mwamuna angathe kulekana naye mkaziyo ndipo kuti atatero sikuti wanyoza lamulo ai. Ana ao sanali kuyembekezeka kukhala ndi mai waoyo ngati anali ndi nthenda yotere. Ngakhale zinthu zimene iye anakhudza zinali kuchedwa zonyansa. Munthu amene anali ndi matenda oterewa sanali kulole-dwa kupembedza Yehova Mulungu mumpingo wa Mulungu ulionse. Anali mkazi wosauka kwambiri ndithu uyu. Sianali wodwala kokha, anali wosafunika. Anali wotaidwa.

Sici cithunzi cace. Kunali Yairo, mkuru wa mzinda, amene anali ndi abwenzi ambiri, ndiponso kunali mkazi wodwala amene analibe abwenzi. Yairo anali ndi mwana wamkazi wa zaka khumi ndi ziwiri amene anali kudwala, mkazi uja anadwala zaka khumi ndi ziwiri. Yesu anali pa ulendo wace kukathandiza Yairo, koma panalibe amene anali pafupi kuti athandize mkazi uyu.

Pamene Yesu anali kuyenda, mwadzidzidzi anaima. "Ndani wandikhuza?" Iye anafunsa. Akuphunzira

anali pafupi kuseka. "Cifuwaniniji", iwo anatero, "mukuona khamu lakuzungulirani, ndipo mutifunsa kuti ndani wakukhudzani"? Akuphunzira aja anauza Yesu kuti cinali cosatheka kufunsa kuti anamukhudza Iye. Koma Yesu anati, "Wina wandikhudza Ine, ndipo kukhudza kumeneko kunali kosiya ndi kukhudza kwa khamuli."

Ndipo pakhamulo ataimilira pafupi ndi Yesu mkaziyo, anayankha, "Ndine ndakukhudzani." anatero iye. Ndipo atagwada pa maso pa Yesu mkaziyo anauza Iye mbiri ya matenda ace ndi cifukwa cace cimene anamkhudzira Iye. Pamenepo Yesu, ndi mtima wodzaza ndi cikondi anati kwa mkaziyo: "Mkaziwe, cikhulukiliro cako cakuciritsa; muka mumtendere, nukhale wocira cibvutiko cako." Ndipo mkazi wobvutika uyu anadwala zaka khumi ndi ziwiri wapeza cikhulukiro ndi kucira mwa Yesu Kristu.

MAPHUNZIRO

1. Yesu siakhala wotanganidwa pakuthandiza munthu amene ali wosowa thandizo. M'ndime izi taona kuti Yesu anali pa ulendo wace wopita kukathandiza Yairo. Koma pamene anaona munthu wina wosowa thandizo Yesu anaima nam'thandiza. Ndi mwa njira imeneyi mmene Yesu afunira ife tikhale. Tiyenera kukhala wotanganidwa ndi nchito ya Mulungu, koma osati kukhaliratu wotanganidwa pakuthandiza anthu amene afuna thandizo.

2. Yesu ali ndi mphamvu yakucita cinthu cimene wina ali yense sangathe kucita. Mkazi wodwala uyu anayesetsa njira iyi ndi iyi. Anapita kwa asing'anga. Anayesa mankhwala amitundu mitundu. Koma zonsezi sizidamucilitsa. Yesu ndiye adamuciritsa mkaziyo. Palibe cinthu cimene cili colephereka kwa Ambuye Yesu.



Pamene anansi ndi abwenzi ace anaona kuti maso a munthuyo anali otseguka ndipo kuti anali kuona bwino anadabwa kwambiri. "Kwacitika ciani," anatero, "Ndani wakutsekula maso ako?" "Munthu wochedwa Yesu," iye anatero. Afarisi anadza ndipo iye anawauza mmene Yesu anatsegulira maso ace. Ndipo anafunsanso makolo ace za cimene cidacitika kwa mwana wao. Sanathe kuzindikira. Ici cingathe kucitika bwanji? Cimene munthu wosaona uja anali kunene ndico kuti Yesu anatsegula maso anga.

Anthu anali wokwiya kwambiri ndi iye kotero kuti anamucotsa munthu amene anali wosaonayo m'Kacisi mwao. Pamene Yesu anamva ici anabweranso kudzalankhula ndi munthuyo. Pamene Yesu anali kulankhula naye Iye anafunsa, "Kodi ukhulupilira mwa Mwana wa Mulungu?" Ndipo munthuyo anati, "Ambuye, iye ndani, kuti ndikhulupilire?" Ine ndine Mwana wa Mulungu," Yesu anatero. Ndipo pamene anayang'ana m'maso mwa Yesu munthuyo anati, "Ambuye, ndikhulupilira."

MAPHUNZIRO

1. Yesu sanali wotanganidwa kwambiri pakulimbana ndi adani ace kuti anayiwala nchito yace. Ici ndi cinthu cacikuru. Nthawi zina Satana amapanga anthu a Mulungu kuti akhale otanganidwa ndi kulimbana kotero kuti sacita zinthu zimene Mulungu afuna kuti iwo acite. Ngati tiyenera kukhala ndi madalitso a Mulungu m'miyoyo yathu tiyenera kukhala wotanganidwa kucita zinthu zimene Mulungu afuna kuti ife ticite.

2. Munthu wakhungu uja anali kufuna kwambiri kuti aone. Moyo wace wonse anakhala wosaona. Sanaona munthu aliyense. Ndipo tsiku lina munthu aika matope m'maso mwace namuuza kuti akasambe. Sanddziwa kuti anali Yesu amene

ife pa Aroma 6:23 kuti "mphotho yace ya ucimo ndi imfa." Koma Buku Lopatulika silitiphunzitsa ife kuti ngati tiona munthu wopunduka kapena wosaona tinene kuti -- munthu ameneyo ali wosaona cifukwa ca cimo lace. Sitinganene kuti pamene tiona munthu wopunduka munthuyo ali wopunduka cifukwa ca cimo limene makolo ace anacimwa. Iai. Buku Lopatulika silitiphunzitsa cimeneci.

Koma tidziwabe, kuti pakanakhala popanda cimo pa dziko lapansi kukanakhala kopanda cobvuta. Koma popeza munthu anacimwa anthu onse abvutika. Pamene Yesu anayankha akuphunzira ace anati, "Munthu uyu siali wosaona cifukwa ca cimo limene anacita. Kapena kuti ali wosaona cifukwa ca cimo limene makolo ace anacita. Iai." Cimo liri gwero la bvuto lace koma simunganene kuti liri la yani.

Atatha kuwauza akuphunzira ace za kuti sanganene kuti munthu ali wosaona cifukwa ca cimo la yani, Yesu anati, "Koma kuti nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye." Yesu sadanene kuti munthu uyu anabadwa wosaona kuti kudzakhale kotero kuti Yesu adzatsegule maso ace. Ici cikadaonetsa kuuma mtima kwa Mulungu, ndipo cikadakhala cosafanana ndi Mulungu kupanga munthu wosaona kuti tsiku lina Yesu akanadza kuno ndi kudzacilitsa munthuyo. Mulungu siali wotero. Muluntu ali cikondi. Siafuna kutipangira zobvuta ife Iye anatuma Yesu ku dziko lapansi kuti adzaticotsere zobvuta.

Pamene Yesu anaona munthu wosaonayo anati kwa akuphunzira ace, "Ino ndi nthawi yakuti Mulungu agwire nchito, ndipo ndiyenera kugwira nchito za Iye wondituma Ine." Pamenepo Yesu analabvula malobvu pansi nakanda thope. Ndipo anatenga thopelo napaka m'maso mwa munthu wosaonayo. Ndi thope m'maso mwace wosaonayo ananyamuka kupita ku thamanda la Siloamu kukasamba monga momwe Yesu anamuuzira.



3. Mkazi uyu anaciritsidwa cifukwa ca cikhulupiliro cace. Cikhulupiliro cipereka dzanja lanu kuti mulandire cimene Yesu angathe kukupatsani. Mkazi uyu anali ndi cikhulupiliro mu mphamvu ya Yesu. Panali wodwala ambiri m'khamu limene lija tsiku limenelo. Zoonadi sianali iye yekhayu amene anali wodwala. Koma iye ndiye amene Buku Lopatulika litiuza kuti anaciritsidwa. Anali munthu wacikhulupiliro. Ngati tifuna kudziwa mphamvu ya Mulungu m'moyo mwathu ifenso tiyenera kukhala ndi cikhulupiliro.

4. Pali kusiyana kwakuru pakati pa kukhala m'khamu la anthu ndi kukhudza Yesu. Pali anthu ambiri amene abwera ku chalichi. Adziwa kupemphera, koma siadziwa mphamvu ya Mulungu m'moyo mwao. Yesu afuna kuti ife timukhudze Iye mwa cikhulupiliro.

5. Mkaziyo ataciritsidwa, Yesu anafuna kuti mkaziyo agawe. Ici ndico cifukwa cace cimene Yesu anafunsira kuti, "Ndani wandikhudza Ine?" Iye anafuna kuti mkazi uja adziwe cimwemwe cimeneci pakuuza munthu wina za madalitso a Mulungu.

MAFUNSO:

1. Cifukwa ciani muganiza kuti mkazi uyu anaciri tsidwa?
2. Cifukwaninji Yesu anafunsa kuti, "Ndani wandikhudza Ine?"
3. Kusiyana kwace nciani pakati pa kukhudza Yesu ndi kungoyenda nao ndi khamu?

-ooOoo-

## PHUNZIRO 5

## YESU NDI ZAKEYU

MAU A MULUNGU: Luka 19: 1-10.

MAU A PA MTIMA:

"Pakuti Mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa cotayikaco."
Luka 19: 10.

### MBIRI YACE

Pa nthawi imene Yesu anakumana ndi Bartimeyu Iye anakumananso ndi Zakeyu. Zakeyu anali mmodzi wa anthu atatu amene anatembenuka mtima Yesu asanafe pa mtanda. Anthu otsilizira atatu amene anatembenuka mtima isanafike imfa ya Yesu ya pa mtanda, anali awa; Zakeyu, Bartimeyu, ndi mbala ija pa mtanda paja. Umu ndimo mmene Yesu anakomanirana ndi Zakeyu.

Yesu anali kupita kupyola Yeriko. Ndipo monga mwa masiku onse, anthu ambiri anali kuyesa kuona Yesu. Kuli konse kumene anayenda anthu anali kumutsata. Anayesetsa kuti angomuona Iye. Mau atangomveka kuti Yesu anali kubwera, khamu linayamba kusonkhana. Pamene anali kupyola Yeriko, anthu anali kuimilira paliponse.

Mmodzi wa anthu amene anafuna kuona Yesu tsiku limenelo anali munthu wamfupi wochedwa dzina lace Zakeyu. Anali wolandira misonkho. Ngakhale kuti anali m'Yuda analikugwira nchito m'boma la Cirona, Iye anali wonyenga pakati pa anthu ace. Cifukwa ca cimeneci anthu sanamukonda. Sanamukonda cifukwa anatenga ndarama zao zonse za msonkho. Boma la



## PHUNZIRO 9

## YESU NDI MUNTHU WOSAONA CIBADWIRE

MAU A MULUNGU: Yohane 9:1-41.

MA A PA MTIMA:

"Ngati sanacokera kwa Mulungu, sakanakhoza kucita kanthu."
Yohane 9:33.

### MBIRI YACE

Phunziro ili lonena za Yesu ndi munthu wosaona ndilo limodzi la maphunziro akuru-akuru m'Buku Lopatulika. Litionetsa ife za cobvuta cace ca cimo, ndipo litionetsa ife cifukwa cace cimene Yesu anadzera kudzakhala pa dziko lapansi.

Tsiku limene Yesu anakomana ndi munthu wosaonayu linali lobvuta. Cifukwa ca mau ace Ayuda anafuna kumponya miyala. Koma asanaponye miyalayo Yesu anacoka mwauzimu m'Kacisimo. Pamene anali kuyenda ndi akuphunzira ace anaona munthu wosaona.

Pamene akuphunzira anaona munthu wosaonayo anayamba kufunsa mafumso. Alikuyang'ana kwa Yesu iwo anati, "Rabi, anacimwa ndani, iyeyu, kapena makolo ace, kuti anabadwa wosaona?" Yesu anawayankha nati, "Sanacimwe ameneyo, kapena makolo ace; koma kuti nchito za Mulungu zionetsedwe mwa iye."

Akuphunzira anafunsa Yesu, "Kodi munthu uyu ali wosaona cifukwa ca cimo lace, kapena cifukwa ca cimo lina limene anacita makolo ace?" Buku Lopatulika litiphunzitsa bwino bwino kuti cimo lidzetsa zowawa ndi zobvuta. Buku Lopatulika litiphunzitsa

Nikodemo anali munthu wacuma. Ndi ndarama zacezo akanatha kugula zinthu zambiri, koma sakanatha kugula cinthu cimodzi cimene iye anali kusowa. Ndarama sizikanatha kugula cikhululukiro ca macimo ace. Anali oweruza. Anali ndi mphamvu ya kuuza anthu kuti acite cimene cinali coyenera kucita. Cifukwa ca malo ace amenewa anthu anamuyang'ana ngati munthu wa pamwamba. Koma ngakhale malo ace a pa ulamulirowa sanakhoze kumupatsa cimene anali kufuna mumtima mwace. Ndarama ndi mphamvu ya ulamuliro sizingathe kukupatsani cimene Yesu afuna kuti inu mukhale nnaco. Njira imodzi yokha yakulandira mphatso kucokera kwa Yesu ndiyo "kubadwa kwatsopano."

MAFUNSO:

1. Kodi citanthauza ciani kunena kuti "kubadwa mwatsopano?"

2. Kodi ndani amene ayenera 'Kubadwa mwatsopano?"

3. Kodi Yesu afuna anthu onse kuti "abadwe mwatsopano?"

-ooOoo-



Ciroma linali kuwauza wolandira misonkhowo ndarama zimene zinali kufunika kucokera kwa anthu. Motero amisonkhowo pa ndarama zonse zimene analandira zopyola pa ciwelengero cofunikaco iwo anali kutenga ndi kukhala zao. Zakeyu anapanga ndarama zambiri ndipo anapanga adani ambiri.

Tsopano iye anafuna kuona Yesu. Koma cifukwa panali anthu ambiri iye sanatha kuona kufika ku njira. Anali munthu wamfupi Kwambiri ndipo sanatha kuona kupyola pa mitu ya anthu amene anali patsogolo pace. Panali cinthu cimodzi cokha coti acite. Ngati akadafuna kuona Yesu pamene anali kupita m'njira adayenera kukwera mumtengo. Ndipo kukwera mumtengo anakwera.

Pamene Yesu anali kupita pa mtengowo anaima. Ndipo anagadama nayang'ana mumtengo. Ndipo pakumuona Zakeyu, Yesu anati, "Zakeyu, tsika, pakuti lero ndipita ku nyumba yako ndi iwe." Anthu anadabwa kwambiri. Sanazindikira cifukwa cakuti Yesu anali kupita kukadya ku nyumba ya munthu wamsonkho. Yesu anali kupita kukadya ndi munthu wocimwa.

Zakeyu anatsika mofulumira mumtengo uja monga momwe akanathera. Yesu anaitana dzina lace. Yesu anamuuza kuti abwere. Ndipo pamene anaimilira pafupi ndi Yesu, iye anati: "Ambuye, gawo limodzi la zanga zonse zogawika pakati ndipatsa osauka, ndipo ngati ndalanda kanthu kwa munthu monyenga, ndim'bwezera kanai."

Yesu anali kumvetsera mau ace ndipo analankhula mau odabwitsa a mtendere. "Lero cipulumutso cagwera nyumba iyi,"anatero Yesu. Ndipo Zakeyu anasanduka ophunzira wace wa Yesu Kristu. Munthu amene ali yense anamuda anasinthidwa pamene Yesu anamkonda iye.

MAPHUNZIRO

1. Pamene Yesu anaitana Zakeyu anabwera. Anali ndi mwai umodzi. Buku Lopatulika likuti, "Yesu anali kupita m'njira." Sitidziwa tidzakhala ndi mimwai ingati. Ncofunika kwambiri kwa yense wa ife kugwiritsa nchito mwai wathu uli wonse kulankhula ndi kugwira nchito ya Yesu.

2. Anthu ayenera kuzindikira kuti Mulungu awafuna iwo ndipo iwo afuna Mulungu. Palibe munthu amene siafunidwa ndi Mulungu. Palibe munthu amene Mulungu siamukonda. Anthu ena angamude koma Mulungu siadana ndi anthu. Mulungu afuna inu ndipo inu mufuna Mulungu. Anthu sanamkonda Zakeyu, koma Yesu anamkonda iye.

3. Mu mbiri iyi Yesu anakweza maso mumtengo ndipo anaona Zakeyu. Koma kawiri kawiri Yesu akweza maso ndipo aona anthu amene ife sitiwaona. Nthawi zonse maso a Yesu ali otseguka kwa anthu amene amufuna Iye.

4. Zakeyu anali munthu wolimba mtima. Anabwera cifukwa anafuna kuona Yesu. Khamu silinamuthandiza. Koma sanayiwala cimene adadzera. Anadza kudzaona Yesu. Njira yokha imene iye akanaonera Yesu inali kukwera mumtengo. Motero iye anakwera mumtengo. Sanacititsidwe ulesi. Kawiri kawiri anthu amanena kuti akonda Yesu amalola zinthu zocepa kuwalepheretsa kufika kwa Ambuye wao kapena ku nyumba ya Mulungu. Koma sikunali kotero ndi Zakeyu.

5. Simungathe kunena za munthu mmene aliri pa maonekedwe ace. Zakeyu anali munthu wacuma cambiri. Kwa anthu ambiri cinaoneka ngati



mphepo iomba kupyola mwa iyo. Koma sitingathe kuiona mphepo. Tikhoza kuona zokha zimene mphepo icita. Tikhoza kuona kuti mphepo ili kuomba. Basi.

Ndipo ndi mau okoma Yesu anayamba kufotokozera Nikodemo kuti cinali cosatheka kuzindikira ndi mtima, zonse za kubadwa kwatsopano. Sizinali zopezeka ndi mtima, koma ndi cikhulupiliro ca mumtima.

MAPHUNZIRO:

1. Pali njira imodzi yokha imene munthu angasandukire mkristu. Ngati munthu afuna kukhala mkristu ayenera "Kubadwanso kwatsopano." Nchito zabwino sizidzatipatsa cipulumutso. Kupita kumapemphero pa tsiku la Sabata liri lonse sikupanga munthu kukhala mkristu. Pali njira imodzi yokha kuti munthu akhale mkristu. Kuti ukhale mkristu ndi kutsata njira ya Yesu uyenera "kubadwa kwatsopano."

2. Anthu onse ali cimodzi-modzi pamene ali pa maso pa Yesu Kristu. Pa mau a Mulungu ena amene taphunzira taona Yesu alikuthandiza anthu amene anali wosauka kwambiri. Taona mmene Yesu anathandizira anthu amene analibe abwenzi. Koma ndi Nikodemo Yesu anali kugwira nchito ndi mmodzi wa oweruza. Yesu analibe kusiyanitsa pamenepa. Yesu aona anthu onse monga momwe aliri. Sapanga anthu ena kuti akhale anthu ena. Afuna anthu akhale monga Iye. Nikodemo anali oweruza wa anthu, koma pamene anadza kwa Yesu iye anali wamacimo woyenera cikhulululukiro ca Mulungu.

3. Ndarama ndi malo aulemu sizipanga anthu kukhala wosangalala. Uyu anali munthu wandarama.

Afarisi anali opembedza koma sianali akristu. Nikodemo anali m'Farisi.

Buku Lopatulka litiuzanso kuti iye anali munthu wacuma. Pa Yohane 19:39 tiuzidwa kuti Nikodemo anadza ndi "zosanganiza za mure ndi aloe monga miyeso zana, kudzoza thupi la Yesu. Munthu wacuma yekha ndiye akanatha kubwera ndi zotero kwa Yesu.

Buku Lopatulika litiuzanso ife kuti Nikodemo anali woweruza wa a Yuda. Anali mmodzi wa atsogoleri ao. Anali kukhala m'bungwe limodzi lalikuru la a Yuda. Anali munthu wofunika kwambiri ---ndipo anafuna kulankhula kwa Yesu.

Atamva kuphunzitsa kwa Yesu naona zocita zace pamene anali kutsogolera anthu Nikodemo anamuka ku malo kumene anali kugona Yesu. Yohane atiuza kuti inali nthawi ya usiku pamene Nikodemo anabwera kwa Yesu. Yesu anamvetsera pamene Nikodemo anali kulankhula ndipo Yesu anamuyang'ana Nikodemo nati, "Nikodemo usowa mtima watsopano, uyenera kubadwanso." Nikodemo anali asanamvenso mau otero kale lonse. Kubadwa kaciwiri? Bwanji? Anali munthu wamkuru. Kukanantheka bwanji kuti abadwenso ngati mwana wakhanda? Pamenepo Yesu anamufotolozera kuti anayenera kubadwa kaciwiri mwa Mzimu wa Mulungu. Adayenera kucoka ku njira za ucimo. Adayenera kukhulupilira mwa Mulungu kuti amupatse mtima watsopano.

Nikodemo anamvetsera, koma sanazindikira. Yesu anadziwa kuti iye sadazindikira. Pamenepo Yesu anamufunsa funso iye. "Nikodemo, kodi udaiona mphepo?" "Iai, sindinaione mphepo", anatero iye. Pamenepo Yesu anayamba kufotokozera Nikodemo. Muli zinthu zambiri m'moyo wathu zimene sitizizindikira. Tidziwa kuti mphepo iomba, cifukwa tikumva mau ace ndipo tingathe kuona mitengo ilikugwedezeka pamene



kuti Zakeyu anali ndi kanthu kali konse; osasowa kanthu Kapena anali ndi nyumba yaikuru. Kapena anali ndi banja labwino. Ndipo ali yense anadziwa kuti iye anali ndi ndarama. Cifukwa Zakeyu anali wolandira ndarama za misonkho. Komabe ngakhale anali ndi zinthu zonsezi sianali wokondwa. Mumtima mwace anali kufunabe cinthu cina. Ndarama zingathe kutigulira zinthu zimene tingazigwire ndi manja athu, koma Yesu yekha angathe kutipatsa cikondi cimene cingathe kudzaza mumtima mwathu.

MAFUNSO:

1. Cifukwa cinai Yesu anadza kudzakhala pa dziko lapansi?

2. Kodi Zakeyu anafuna kucita ciani atasanduka mkristu?

3. Kodi cimene cakucititsani cidwi kwambiri ndi ciani pa mbiri ya Zakeyu?

-ooOoo-

## PHUNZIRO 6

### YESU NDI WAKHATE

MAU A MULUNGU: Mateyu 8:1-3; Marko 1: 40-45; Luka 5: 12-15.

MAU A PA MTIMA:

"Ndipo Yesu, anagwidwa cifundo, natansa dzanja lace, namkhudza iye, nanena naye, Ndifuna; khala wokonzedwa."
Marko 1:41.

### MBIRI YACE

Khate ndi nthenda yoipa kwambiri. Ndi imodzi ya nthenda zoipitsitsa zimene anthu angakhale nazo. Lero, tingathe kukhala woyamika kuti asing'anga anapeza mankhwala okhoza kucilitsa nthenda ya khate. M'masiku akumbuyoku pamene Yesu anakhala pa dziko lapansi lino sanadziwa mankhwala ociritsa nthenda ya khate.

Pamene munthu anayamba kukhala ndi nthenda imeneyi zotupatupa zinaoneka pa khungu, thupi lonse. Ndipo zotupatupa izi zinasanduka zofiira ndipo khungu la pa thupi likhala louma. Pamene thupi linayamba kuuma linasanduka loyera. Mutu unakhala wouma kwambiri ndipo tsitsi linayamba kuthothoka. Ndipo pamene nthendayi inali kufika poipitsitsa zala za kumanja ndi za kumwendo zinayamba kuduka m'fundo mwace. Inali nthenda yoipadi kwambiri.

Kuonjezera pa uluru wa nthendayi munthu wodwala khate anali kucotsedwa m'mudzi nasungidwa kunja kwace kwa mudzi. Cili conse cimene iwo anakhudza cinasanduka coipa. Sanali kumwera cikho comwe anthu ena



## PHUNZIRO 8

### YESU NDI NIKODEMO

MAU A MULUNGU: Yohane 3: 1-21; 7: 50-52; 19: 39.

MAU A PA MTIMA:

"Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu."
Yohane 3:3.

### MBIRI YACE

Yesu anali m'mudzi wa Yerusalemu pa nthawi ya Pasika. Munali anathu ambirimbiri mu Yerusalemu cifukwa ca Pasika. Anamva Yesu alinkulankhula ndipo anaona zocita zace pamene anatulutsa osintha ndarama aja m'Kacisi muja. Ambiri a iwo anamva za zizindikiro zadabwitsa zimene Iye analikucita. Cifukwa ca mau ace anamkhulupilira Iye. Ambiri a iwo anali ndi mafunso pamene anamva mau ace.

Mmodzi wa anthu amene anali ndi mafunso anali munthu wina dzina lace Nikodemo. Nikodemo anali munthu wamkutu - wofunika. Buku Lopatulika litiuza kuti iye anali m'Farisi. Afarisi ndiwo anali anthu opembedza pa nthawi imene Yesu anadza ku dziko lapansi. Koma pali kusiyana pakati pakukhala munthu wopembedza ndi kukhala wodziwa Yesu. Ungathe kukhala munthu wopembedza koma osakhala mkristu. Kunena kuti munthu ali wopembedza ndiko kunena kuti akhulupilira m'cinthu cina. Anthu amene akhulupilira Cinasala ali opembedza koma siakristu. Anthu okha amene akhulupilira mwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi wao ndiwo akristu.

MAFUNSO:

1. Kodi muganiza kuti cinthu cacikuru ndi citi m'ndime zimene taphunzira lerozi?

2. Kodi Yesu afuna kuti mucite ciani ndi moyo wanu?

3. Kodi mudabwerapo ndi anzanu ena nthawi ina kuti adzamve mau a Yesu?

-ooOoo-



anali kumwera. Sanali kufunda zofunda zomwe ena akanafunda. Cili conse cimene iwo anacikhudza cinali kutaidwa.

M'malo mwakuti asamakumane ndi anthu anali kubvekedwa belu m'khosi mwao. Pali ponse pamene munthu wina anadza pafupi ndi iwo anaimba belu ndi kufuula kuti :wonyansa." Anthu amene anali ndi khate anali ndi moyo wobvutadi. Panalibe amene anali kuwafuna ndipo panalibe amene anawathandiza. Anali wotaidwa.

Ciphunzitso cacitali kwambiri cimene Yesu analalikira cinali ciphunzitso ca pa phiri. (Cili pa Mateyu) mitu ya 5, 6, 7. Yesu anangotsiliza kulalikira ciphunzitso cimeneci ndipo anali kutsika kucokera ku phiri. Anthu ambiri anali kumutsatira. Anali asanamve mau okhala ngati amene Iye analankhula kwa iwo. Ndipo mwadzidzidzi munadza munthu wakhate m'khamulo. Pamene anali kuyenda kudza kwa Yesu, iye anati, "Ambuye, ngati mufuna, mungathe kundikonza."

Pamene Yesu anamuyang'ana iye mtima wace unadzazidwa ndi cikondi. Buku Lopatulika linena kuti, "Iye anagwidwa ndi cifundo." Yesu sanaona munthu amene sanamukonda. Ndipo pamenepo Yesu anatansa dzanja lace nakhudza wakhate uja ndipo anati, "Ndifuna, khala wokonzeka." Ndipo m'wamsanga, nthawi yomweyo, khate lace linacoka. Anacoka mabanga oyera aja. Zinacoka zironda zija. Munthuyo anaciritsidwa. Moyo wace unakhalanso wangwiro. Cinthu codabwitsa pa cimeneci ndico kuti Yesu anamkhudza iye. Ici sicimene anthu akanacita. Ndani akanakhudza munthu wakhate? Ndani akanatansa dzanja lace labwino ndi kukhudza nalo thupi la amene anali ndi nthenda yoopsa ya khate? Yesu yekha. Yesu yekha.

Pamenepo Yesu anamuuza kuti apite kwa ansembe ndi kukacita zinthu zimene Mose analamulira. Kuti

mudziwe zimene Mose analamulira anthu kuti azicita kuti ayeretsedwe khate welengani Levi tiko 14: 4-32. Izi ndizo zimene lamulo linawauza kuti azicita. Koma palibe mmodzi yense amene anacilitsidwa mwa macitidwe amenewa. Munthu yekha amene anacilitsidwa khate m'Cipangano ca Kale anaciritsidwa mwa njira yozizwitsa ---osati mwa njira iyi ai.

MAPHUNZIRO:

1. Palibe munthu amene ali ndi nthenda yaikuru yosatha kubwera nayo kwa Yesu. Anthu angathe kuona munthu nanena kuti munthu ameneyo ali wa ubve, koma Yesu siatero. Yesu anati: "Iye amene adza kwa Ine sindidzamtaya kunja." Yesu aona anthu monga mmene ayenera kukhalira; osati monga mmene aliri. Wina ali yense angathe kunena kuti ali walitsilo, koma Yesu siatero.

2. Pa Yesu damulo lalikula nthawi zonse linali la cikondi. Yesu anali wosiyana ndi anthu ena onse. Kwa Yesu malamulo onse a mwambo wa m'Cipangano ca Kale anapereka njira ya lamulo la cikondi. Potsiliza pace mu utumiki wace Yesu anauza ophunzira kuti malamulo onse akanaphatikizidwa pa malamulo awiri. Loyamba "Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse," ndi "Uzikonda mnansi wako monga udzikonda iwe mwini." Cikondi cikwanilitsa malamulo onse.

3. Taonani pang'ono pa cikhulupiliro cimene anali naco wakhate uja mwa Yesu. Panalibe cikaikilo mumtima mwa wakhate uja pa zamphamvu ya Yesu kuti akanamucilitsa. Pamene anadza kwa Yesu anati: "Ngati mufuna." Cimwemwe cotani cimene tikadakhala ndi cikhulupiliro ca mtundu uwu mwa Yesu. "Ngati ukhulupilira, zinthu



ambiri amene adziika pa okha modzipatula. Nthawi zina anthu ena siakonda anthu a pfuko lina. Nthawi zina anthu siakonda anthu a mtundu wina. Ngati tikhala odzikonda tokha sitingathe kukhala monga mmene Yesu afunira kuti ife tikhale. Kudzipatula ndiko cidani. Sitiyenera kukhala ndi cidani m'mitima yathu ngati tili ndi cikondi ca Yesu m'mitima yathu.

3. Ali yense ali ndi cinthu coti apereke kwa Yesu. Mkazi wa ku Samariya uyu anakhala ndi moyo wocimwa. Sadatsata njira za Mulungu m'moyo mwace. Koma ngakhale kuti moyo wace unali wodzaza ndi cimo ----anali ndi cinthu copereka kwa Yesu. Yesu anafuna kuti mkaziyo apereke kwa Iye mtima wace. Munthu ali yense ali ndi cinthu coyenera kupereka kwa Yesu. Yesu afuna kuti ife tipereke mitima yathu kwa Iye.

4. Yesu aona zotheka zonse m'moyo wa ali yense. Anthu a m'mudzi muja sadamkonda mkazi wa zoipa uja. Koma Yesu anaona zotheka mwa mkazi uja. Atapeza Yesu kuti ndiye Mesiya iye anathamanga kupita ku mudzi ndi kukauza anthu. Cifukwa ca umboni wace anthu onse a m'mudzi muja anabwera kudzamva mau a Mwana wa Mulungu. Tisamayang'ana kwa anthu ena ndi kuganiza kuti sangathe kucita kanthu. Pamene Yesu anadza mumtima mwa munthu apereka mphamvu yakucita nayo zinthu zace.

5. Nthawi ya kunyamula uthenga wabwino wa Yesu kufika nao kwa anzathu ndi tsopano lino. Ngati tipita kukauza ena za Yesu anthu adzabwera kudzamva mau ace.

m'Samariya. Koma mkazi uja sadawaona akuphunzirawo. Mtiam wace unagunda pamene anamva kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu kotero kuti anasiya mtsuko wace nathamangira ku mudzi. Anafuna kuti anthu onse m'mudzi wacewo adziwe kuti Yesu anali kumeneko. Anathamanga m'njira zonse kuuza anthu, "Ndampeza Mesiya, ali kuno, tiyeni ndi ine."

Ndipo iwo anabwera. Anthu onse a m'mudzimo anamtsata iye pamene iye anabwerera ndi liwilo kupita ku malo amene Yesu anali kudikira. Pamene Yesu anakweza maso naona anthu akutsata mkazi uja Iye anatembenukira kwa akuphunzira ace nati: "Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onai ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta." Iye anali kuuza akuphunzira ace kuti mitima ya anthu inali ndi njara tsopano kuti amve mau a Ambuye. Zili cimodzimodzi ndi lero. Pamene munthu mmodzi auza anthu ena za cikondi codabwitsa ndi cikhululukiro codabwitsa ca Yesu enawo atsatira.

MAPHUNZIRO

1. Pamene Yesu anakomana ndi mkazi wa ku Samariya anali wblema ndi wanjara. Anayenda ulendo wautali, koma sanali wotopa kolephera nako kuthandiza munthu amene anali wosowa thandizo. Nthawi zambiri timaganiza kuti tili otopa kwambiri kuti sitingathe kupita ndi kukalankhula mau a Yesu. Nthawi zambiri anthu amabwera ku nyumba yathu ndipo asowa thandizo. Timacita ciani? Kodi tiwauza kuti talema kwambiri? Kodi tiwathandiza? Yesu anayesetsa ndi mtima wace wonse Kodi inu mumatero?

2. M'dziko lapansi limene tikhalamo lino kuli anthu



zonse zili zotheka."

4. Lamulo linanena kuti ngati wina akhudza munthu wakhate atenga khate, Koma Yesu anamukhudza. Ici ndi cithunzithunzi codabwitsa. Yesu anangotsiliza kuphunzutsa akuphunzira ace ndi anthu ena za malamulo atsopano a Ufumu wace. Anauza anthu kuti njira yace inali yobvuta. Anawauza kuti acitire ena zabwino kuposa mmene lamulo linenera. Anawauza kuti akhale citsanzo ku dziko lapansi. Ndipo tsopano pamene Iye anali kutsika kucokera pa phiri wakhate anathamanga kukumana naye. Ndipo Yesu anaonetsa anthu kuti Iye angathe kucita zinthu zimene anawauza kuti azicita.

5. Ngati inu ndi ine tifuna kukhala monga Ambuye wathu Yesu tiyenera kutenga anthu kumene tiwapeza ndipo ticite zonse zimene tingathe kuti tiwathandize kuti akhale anthu abwino ndithu. Ife sitili kuno kupereka malamulo kwa anthu. Ife tili kuno kuonetsa kwa anthu cikondi ca Mulungu mwa Yesu Kristu.

MAFUNSO:

1. Ndi ciani cimene Yesu anacita kwa wakhate cimene cinali cacilendo?
2. Ndi cinthu citi cacikuru cimene tingathe kucita kwa anthu ena?
3. Kodi Yesu akonda anthu onse? Kodi mwawauza iwo za cikondi cace?

-ooOoo-

## PHUNZIRO 7

## YESU NDI MKAZI WA KU SAMARIYA

MAU A MULUNGU: Yohane 4: 1-35.

MAU A PA MTIMA:

"Mulungu ndiye Mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mu mzimu ndi m'coonadi."
Yohane 4:24.

### MBIRI YACE

Yesu anali wolema kwambiri. Dzuwa linakwera pamwamba ndipo miseu inali ndi fumbi. Linali tsiku lotentha pamene Yesu anayenda kufika ku citsime cimene cinali codziwika ngati citsime ca Yakobo. Atagwidwa ndi ludzu pa ulendo wace Yesu anakhala pansi pa citsime. Sipanapite nthawi yaitali mai wa ku Samariya anadza kudzatunga madzi pa citsimepo. Yesu anali yekha pamene mkaziyo anadza kudzatunga madzi. Anali yekha cifukwa akuphunzira ace anapita ku mudzi kukagula cakudya.

Pamene mai uja anayamba kutsila madzi mumtsuko wace kucokera pa citsimeco Yesu anamupempha kuti amupatse madzi amwe. Mkaziyo anadabwa kwambiri. Yesu anali m'Yuda. Mkaziyo anali m'Samariya. Ndipo m'masiku amenewo m'Yuda sanali kulankhula kwa m'Samariya. Mkazi uja anayang'anitsitsa kwa Yesu nati, "Bwanji Inu, muli m'Yuda, mupempha ine kuti ndikupatseni madzi mumwe, ndine m'Samariya?"

Mwacifundo Yesu anayankha mkaziyo nati; "Ngati ukadadziwa kuti Ine ndine yani ukadandipempha madzi kuti umwe, ndipo ndikadakupatsa madzi amoyo." Alikuyang'ana kwa Yesu mkaziyo anafunsa Yesu mmene



akadamupatsira madzi pamene analibe cotungira madzi. Pamenepo Yesu anamufotokozera kuti madzi amene Iye anali kunenawo anali madzi a moyo. Madzi a moyo amene akanadzaza mtima ndi madalitso ndi ubwino wa Mulungu. Anali madzi a cikhululukiro amene Mulungu anapereka kwa iwo amene anamkondza. "Ambuye, ndipatseni madzi amenewo," anatero mkaziyo.

Pamene ananena mau awa Yesu anayamba kukamba naye za moyo wace wamkaziyo. Mkazi uyu anali ndi moyo wasasangalala. Anakwatiwa kasanu. Ndipo nthawi imeneyi anali ndi mwamuna amene sianali mwamuna wace. Anthu akumene anali kukhala iye sanamkonda. Akadakhala kuti analoledwa ndi anthu m'mudzimo sibwenzi alikutunga madzi nthawi ya masana. Akazi am'mudzimo anali kutunga madzi pa nthawi ya mmawa ndi nthawi ya madzulo. Koma iye anabwera yekha pa nthawi ya pamsana kudzatunga madzi. Analibe abwenzi m'mudzimo Anali mkazi wocimwa ndipo azimai ena sanamkonda. Koma Yesu anamkonda.

Mkaziyo anamvetsera mau ali onse amene Yesu ananena. Anamvetsera mau ali onse amene Iye ananena za moyo wace, ndipo anamvetsera pamene anali kukamba za kupembedza Mulungu. Iye anauza mkaziyo kumene akanatha kupeza Mulungu. Masiku apitawa, anatero Iye, anthu anali kupita ku malo kwina ndi kwina kukapembedza Mulungu. Koma tsopano, angathe kupembedza Mulungu m'mitima yao kuli konse kumene ali. "Pakuti Mulungu ndi Mzimu ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'coonadi." Kupembedza koonadi kucokera mumtima. "Ukhulupilire mau amene ndikuuza iwe," Yesu anatero, "cifukwa Ine ndine Mesiya amene mwakhala muli kuyembekezera."

Pamene Yesu analikunena izi akuphunzira anafika. Pamene anaona Yesu alikulankhula ndi mkazi anadabwa kwambiri. Anadabwa cifukwa Yesu anali kulankhula ndi